# PHUNZIRO LA 25

1. Kodi amene amkamutchinjiriza Yakobo mpaka ku-mubweretsanso kwawo ku Kanani kuchokera ku Harani anali ndani?
-Mulungu.

2. Kodi dzina la mwana wa Yakobo amene amkamukonda kwambiri kuposa ana ake ena onse linali ndani?
-Yosefe.

3. Chifukwa chakuti Yakobo amkamukonda kwambiri Yosefe kuposa abale ake ena onse, kodi abale ake a Yosefeyo amkamuganizira chiyani iye?
-Iwo amkamuchitira msanje, ndiponso amkamuda kwambiri iye.

4. Kodi maloto oyamba amene anapereka Mulungu kwa Yosefe anali otani?
-Mitolo ya tiligu ya abale ake a Yosefe, inaŵeramira mtolo wa tiligu wa Yosefe.

5. Kodi maloto achiŵiri amene Mulungu anapereka kwa Yosefe anali otani?
-Dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi khumi ndi imodzizo zi-namuŵeramira Josefe.

6. Kodi maloto onsewo amkatanthawuza chiyani?
-Tsiku lina, Mulungu adzamupatsa ufumu Yosefe, ndipo onse a m'banja lake adzamugwadira iye.

7. Kodi amene amkadziŵa za tsogolo la Yosefe ndiku-muwonetsa Yosefeyo tsogolo lakelo kupitira m'maloto anali ndani?
-Mulungu.

8. Kodi Mulungu amadziŵa zinthu zingati za tsogolo lathu?

-Mulungu amadziŵa zonse za tsogolo lathu.

9. Kodi abale ake a Yosefe anachita naye chiyani Yosefe atafika kudzaŵawona kumene amkadyetsera ziweto zawo kuja?
-Poyamba anamuvula mkanjo wake, namuponya mu chitsime chopanda madzi.
-Kachiŵiri abale ake a Yosefe anamugulitsa iye ngati kapolo kwa anthu a malonda a ukapolo.

10. Kodi anthu a malonda a ukapolowo anamutengera kuti Yosefe?
-Ku Ejipito.

11. Kodi anthu a malonda a ukapolo aja anamugulitsa Yosefe kwa ndani?
-Kwa Potifala.

12. Kodi chinachitika kwa Yosefe ndi chiyani pamene iye anali ngati kapolo wa Potifala?
-Mkazi wake wa Potifala anamunamizira Yosefe, ndipo Potifalayo anamuyika Yosefe mnyumba ya ukayidi.

13. Kodi amene amkamuyang'anira Yosefe mynumba ya ukayidiyo anali ndani?
-Mulungu.

-Kodi Mulungu anayiŵala za Yosefe?
-Iyayi.

-Mulungu samuyiŵala wina aliyense.

-Yosefe ali mnyumba ya ukayidi ku Ejipito.
-Dzina la mfumu wa ku Ejipitoko linali Falawo.

-Tsiku lina, Mulungu anapereka maloto kwa Falawo, mfumu ya ku Ejipito.



Yosefe ali ndi moyo. Ndipita ndikamuwone ndisanafe."

-Chomcho bambo ake a Yosefe ndi abale ake aja anapita kukakhala ndi Yosefe ku Ejipito.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 46:5-7

5-Tsopano Yakobo ananyamuka kuchokera ku Beereseba. Ana ake a Isilayeli aja anaakweza bambo awo, yakobo, pamodzi ndi akazi ndi ana pa ngolo zimene Farawo anazitumiza.
6-Anatenga zoweta zawo zonse pamodzi ndi zinthu zonse zimene anali nazo ku Kanani, ndipo anapita nawo ku Ejipito. Yakobo anatenga anthu ake zonse.
7- Anaatenga ana ake onse pamodzi ndi zidzukulu zake zonse.

-Zaka zambiri zapitazo, Mulungu anamuwuza Abulahamu kuti zidzukulu zake zidzapita ku Ejipito.

-Patatha zaka zambiri, Mulungu ankachita zimene Iye analankhulazo.

-Mulungu adzachita zonse zimene walankhula.

-Chifukwa chakuti kunali njala yayikulu, Yosefe anaapepha abale ake aja kuti abwerere ku Kanani, ndipo akaatenga bambo awo pamodzi ndi banja lawo lonse kupita nawo ku Ejipitiko.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 45:9-11

9-Tsopano fulumirani bwererani kwa bambo anga, mukaawuze kuti mwana wanu Yosefe akuti, “Mulungu wandikuza mpaka kukhala olamulira Ejipito yense, tsopano bwerani kuno musachedwe. “

10-Mungathe kudzakhala kuno ku dziko la Goseni, kuti mukhale pafupi ndi ine. Mudzakhale kuno inuyo, ana anu, zidzukulu zanu, nkhosa zanu, mbuzi zanu, ng’ombe zanu pamodzi ndi zonse zimene muli nazo.

11-Mukadzakhala ku Goseni, ine ndidzidzakusamalirani. Zaka za njala zikanalipobe zisano. Sindikufuna kuti inu musawuke pamodzi ndi banja lanu, ndi onse amene muli nawo.”

-Abale ake a Yosefe aja anabwelera ku Kanani.

-Imvani zimene anamuwuza Yokobo, bambo awo:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 45:25-28

25-Tsopani iwo anachoka ku Ejipito, kubwerera ku Kanani kwa bambo awo Yakobo.

26-Atafika anaawuza bambo awo kuti, “Yosefe ujatu ali moyo! Ndi amene akulamulira Ejipito yense!” Yakobo anachita ngati wakomoka, pakuti sanazikhulupilire zonena zawozo.

27-Komabe iwo atamuwuza zonse zimene Yosefe anaawuza, ndiponso atawona ngolo zimene Yosefe anatumiza kuti iye akwere popita ku Ejipito. Yakobo anayamba kutsitsimuka.

28-Ndipo anati, “Basi chabwino, mwana wanga



Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:1-4

1-Patapita zaka pang’ono Falawo analota atayipa mphepete mwa mtsinje wa Nayilo.

2-Nthaŵl yomweyo anangowona ng’ombe zisano ndi ziŵiri zonenepa bwino zikutuluka mu mtsinjemo, ndikuyamba kudya msipu wa m’mabango.

3-Kenako mu mtsinje momwemo munatulukanso ng’ombe  zisano ndi ziiri zowonda ndiponso zofowoka, zimene zinayima pa mtunda pafupi ndi ng’ombe zina zija.

4-Tsopano ng’ombe zowonda zija zidadya zimzake zonenepa zija.Pamenepo Falawo anadzuka.

-Kodi ndi maloto otani amene Mulungu anaapereka kwa Farawo?
-Ng’ombe zisano ndi ziiri zowonda zinadya ng’ombe zisano ndi ziiri zonenepa.

-Usiku omwewo, Mulungu anamupatsa Farawo maloto achiiri.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:5-8

5-Atagonanso analotanso maloto ena. Adawona ngala za tiligu zisano ndi ziŵiri zitabala pa phesi limodzi, zinali zakucha ndiponso zokhwima.

6-Kenako panaphukanso ngala zina zisano ndi ziŵiri zofwapa ndi zopserera ndi mphepo ya mkuntho ya ku vuma.

7-Ngala zofwapazo zinameza ngala zisano ndi ziiri zokhwima zija. Falawo atadzuka anawona kuti anali maloto chabe.

8-Kutacha m’maa anavutika kwambiri, mwakuti anaayitana a matsenga ake onse ndi anthu a nzeru onse a ku Ejipito. Onsewo atabwera, Falawo anaafotokozera maloto akewo, koma panalibe ndi m’modzi yemwe amene

anatha kuamasulira.

-Kodi maloto achiŵiri amene Mulungu anapereka kwa Yosefe anali otani?
-Masache asano ndi airi owonda a tirigu anadya masache asano ndi airi onenepa a tirigu.

-Mulungu ankalankhula ndi Farawo m'maloto ake.

-Kodi masiku ano Mulungu amalankhula bwanji ndi anthu?
-Masiku ano Mulungu amalankhula ndi anthu kupitira mu Buku Lake, Bayibulo.

-Farawo anali mfumu ya ku Ejipito koma iye sankakhulupilira mwa Mulungu.

-Farawo ndi anthu ake ankapembedza dzua, mwezi ndi nyenyezi.
-Farawo ndi anthu ake ankapembedzanso nyama ndi achule.
-Farawo ndi anthu ake ankapembedzanso mtsinje umene unali m'dziko lawo.

-Ngakhale kuti Farawo sankamukhulupilira Mulungu, kodi Mulungu anakamutsogolelera Farawo kuti achite zimene Mulunguyo ankafuna?
-Inde.

-Mulungu ndi Mulungu, ndiponso Mulungu amatha kuatsogolera anthu kuti achite zimene Mulunguyo akufuna.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri, zinthu zonse zimene amachita Mulunguyo kwa anthu zimakhala zabwino.

-Amuna onse a nzeru a mu Ejipito sanaadzie matanthawuzo a maloto a Farawo.



chifukwa chakuti anthu amenewa adya ndi ine masana ano."
17-Wantchitoyo anachita monga m'mene Yosefe anamuwuzira, napita nawo abale ake aja ku nyumba kwa Yosefe.

-Pamene Yosefe ndi abale ake aja anali pamodzi, Yosefe anazibisa kwa abale akewo kuti iyeyo anali Yosefe.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 45:3-8

3-Yosefe anaawuza abale ake aja kuti, "Ine ndine Yosefe. Kodi bambo anga akadali ndi moyo? Koma abale akewo anadzadzidwa ndi mantha, kotero kuti sanathe nkumuyankha komwe.
4-Tsopano Yosefe anaawuza kuti, "Chonde senderani pafupi." Onse atabwera pafupi, Yosefe anati, "Ine ndine m'bale wanu uja Yosefe, amene munandigulitsa ku Ejipito.
5-Koma tsopano musataye mtima kapena kuvutika, popeza kuti Mulungu mwini wake ndi amene ananditumiza kuno, chomcho kuti apulumutse moyo wanu.
6-Chaka chino ndi chaka chachiiri cha njala. Koma zatsalabe zaka zina zisano, ndipo pa zaka zimenezi anthu sadzalima kapena kukolola.
7-Mulungu ananditumiziratu ine kuno kuti ndikupulumutseni, chomcho kuti ziwoneke zidzukulu zanu zambiri.
8-Chomcho sindinu amene munanditumiza ine kuno ayi, koma Mulungu. Iye wandisandutsa nduna yayikulu ya Farawo. Dziko lonse lino lili m'manja mwanga. Ejipito yense ndikulamulira ndi ine.

-Kodi Yosefe analankhula chiyani kwa abale ake aja?

-Yosefe analankhula kuti Mulungu yekha ndi amene anamutumiza iye ku Ejipitiko.

kuti, “Pitaninso, mukatigulire chakudya pang’ono.”

3-Koma Yuda anati, “Munthu uja anatichenjeza kolimba kuti sadzatilolanso kuwonekera pa maso pake, tikapanda kupita naye mng’ono wathuyu.

4-Mukatilola kuti timutenge, tipita kukakugulirani chakudya.

5-Mukapanda kulola, ife sitipita, popeza kuti munthu ameneyo ananeneratu kuti, “Sindidzakulorani kufika pa maso panga mukadzapanda kubwera naye m’bale wanuyo.”

11-Tsopano bambo awo, Isilayeli, anaŵawuza kuti, “Ngati ndi m’mene zilili, chitani chomcho. Munthuyo mutengereniko zipatso zokoma za m’dziko lino m’matumba mwanu kuti mukamupatse. Mumtengerenso mafuta odzola pang’ono, mafuta onunkhira osiyanasiyana , mure, mtedza, ndiponso zipatso zinanso.

12-Mutenge ndalama zokwanira, kuti mukabweze ndalama zimene zinapezeka m’matumba mwanu zija. Makamaka zinthu zinali zitalakwika.

13-Mutengeni m’bale wanuyu ndipo nyamukani, mupitenso kwa munthuyo.

14-Mulungu Mphambe akuchitireni chisoni pa maso pa munthuyo, kuti abweze m’bale wanu wina uja pamodzi ndi Benjamini. Ngati ana anga onse andifere, andifere basi.”

-Abale ake a Yosefe anapitanso ku Ejipito kuja.

-Atafika ku Ejipitiko, Yosefe anaayitanira ku nyumba kwake abale akewo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 43:16-17

16-Yosefe atawona Benjamini, anamuwuza wantchito oyang’anira zonse pa nyumba pake kuti, “Anthu aa aloetse mnyumba.  Ndipo uphe nyama ndi kuyiphika bwino,



-Koma anthu ena anamuwuza Farawo kuti Yosefe ndi amene angathe kumasulira maloto a Farawowo.

-Chomcho, Farawo anatumiza uthenga wakuti amutulutse Yosefe mnyumba ya ukayidi ndipo abwere naye kwa iye.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:14-16

14-Tsopano Falawo anamuyitanitsa Yosefe, ndipo anamutulutsa msanga ku ndendeko. Iyeyo atameta bwino ndi kusintha zovala, anapita kwa Falawo kuja.

15-Falawo anamuwuza Yosefe kuti, “Ine ndinalota maloto, koma palibe ndi m’modzi yemwe amene akutha kumasulira malotowo. Tsopano anandiwuza kuti iwe ukamva maloto, umatha kumasulira kwake.”

16-Yosefe anayankha kuti, “Sindine ayi, koma Mulungu ndi amene adzatha kuyimasulira mfumu maloto amenea."

-Yosefe anadzia kuti iye sangathe kumasulira maloto a Farawo.

-Komanso iye anadzia kuti akhoza kudzia matanthawuzo a maloto a Farawo.

-Chifukwa chakuti Yosefe ankamukhulupilira Mulungu, Mulungu anamuwululira matanthawuzo a maloto a Farawo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:25-32

25-Apo Yosefe anawuza Falawo kuti, “ Maloto onse airia ali ndi tanthawuzo limodzi lokha. Mulungu wakuwuziranitu zimene adzachite.

26-Ng’ombe zisano ndi ziiri zinenepazo ndi zaka zisano ndi ziiri. Ndipo ngala za tiligu zisano ndi ziiri zokhwimazo, nazonso ndi zaka zisano ndi ziiri. Kumasulira

kwake ndi kumodzi.
27-Ng'ombe zisano ndi ziiri zowonda zimene zinabwera pambuyo zija, ndiponso ngala za tiligu zisano ndi ziiri zopserera ndi mphepo ya ku vuma zija, ndi zaka zisano ndi ziiri za njala.
28-Tsopano monga m'mene ndanenera kale muja, ndiye kuti Mulungu wakuwuziranitu zomwe adzachite.
29-Padzakhala zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri m'dziko lonse la Ejipito.
30-Patapita zaka zimenezo, padzakhalanso zaka zisano ndi ziiri za njala, ndipo zaka zonse zija za zokolola zambiri zidzayialika mu Ejipito monse. Njalayo idzawononga dziko.
31-Zaka zonse zija za zokolola zambiri sizidzakumbukikanso, chifukwa chakuti njala imene idzabwereyo idzakhala yowoopsa.
32-Poti inu Falawo mwalota kairi maloto okhaokhaa, zikuwonetsa kuti Mulungu ndi amene wakonza zimenezi, ndipo azichitadi posachedwa.

-Kodi ndani amene anamupatsa Yosefe nzeru zakutha kumasulira maloto a Farawo?
-Mulungu.

-Kodi maloto aŵiriwa ankamasulira chiyani?
-Zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri zidzadyedwa ndi zaka zisano ndi ziiri za njala.

-Kwa zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri ndi zaka zisano ndi ziiri za njala, Yosefe ankapereka nzeru kwa Farawo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:33-36

33-Tsopano inu mfumu sankhani munthu wodzia zinthu ndiponso wa mzeru, mumupatse ulamuliro pa dziko lonse la Ejipito.
34-Musankhenso akuluakulu m'dziko lonse lino,



-Kodi chifukwa chiyani Yosefe anaakhazika mwa nkhaza abale ake aja ndikuatsekera mnyumba ya ukayidi?
-Yosefe ankafuna kuti abale akewo aganizire zimene ankamuchita iye ali wamng'ono.

-Patatha masiku atatu, Yosefe anaasiya abale ake aja kuti atuluke mnyumba ya ukayidiyo ndipo anamusiya m'modzi.

Apa pali zimene analankhula Yosefe kwa abale ake aja:

Tiyeni tierenge Genesesi 42:18-20

18-Patapita masiku atatu, anaawuza kuti, "Ine ndimawopa Mulungu. Chomcho ndikupatsani mwayi wuwupulumutsa moyo wanu mukachita izi.
19-Ngati inu muli okhulupirika, mmodzi yekha atsalire mu ndendemu, ena nonsenu mungathe kumapita, kuti mukapereke tirigu amene mwagulayu ku banja la kwanu kuli njalako.
20- Mng'ono wanuyo mukabwere naye kuno, kutsimikiza kuti mukunenadi zowona, ndiponso simudzaphedwa." Iwo anavomereza zimenezo.

-Yosefe anaapatsa abale ake aja zakudya, ndipo anaatumiza onsewo ku Kenani koma m'modzi anatsala ku Ejipitiko.

-Patapita nthai, zakudya zimene anakatenga abale ake a Yosefe aja zinantha.

-Chomcho bambo ake a Yosefe anaawuza ana ake amuna aja kuti apitenso ku Ejipito kukagulanso zakudya zina.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 43:1-5 ndi 11-14

1-Njala idakula kwambiri mu dziko la Kanani.
2-Tsopano banja la Yakobo litadya tirigu yense amene anakagula ku Ejipito uja, Yakobo anaawuza ana ake aja

6-Chomcho abale ake aYosefe nawonso anabwera, ndipo anamugwadira Yosefeyo, namuŵeramira.

7-Yosefe ataŵawona abale akewo, anaazindikira, koma anangochita ngati kuti sanaadzie. Anayamba kualankhula mozaza, naafunsa kuti, “Kodi inu mukuchokera kuti?” Iwo anayankha kuti, “Tikuchokera ku Kanani, tadzagula chakudya kuno.”

8-Yosefe anaazindikira abale ake aja, koma iwo sanamuzindikire.

9-Anaakumbukira maloto aja onena za iwo, ndipo anati, “Ndinu anthu ozonda dziko. Mwabwera kuno kudzazonda kuti mowone ngati dziko lathu ndi lofowoka.”

10-Iwo anayankha kuti, “Iyayi mbuye wathu, ife atumiki anu tabwera kuno kuti tidzagule chakudya basi.

11-Tonsefe ndife pachibale. Sindife azondi, mbuye wathu, koma ndife anthu okhulupilira ndithu.”

12-Yosefe anati, “Iyayi, inu mwabwera kudzazonda dziko lathu kuti muwone ngati ndi lofowoka.”

13-Tsopano iwo anati, “Mbuye wathu, ife tinalipo ana amuna khumi ndi airi pachibale pathu, bambo wathu mmodzi, ku dziko la kwathu ku Kanani. Wamng’ono ali ndi bambo wathu ndipo wina anamwalira.”

14-Koma Yosefe anaayankha kuti, “Paja ndanena kale kuti ndinu azondi basi.

15-Tsopano ndikuyesani motere; ndikulumbira kuti pali Farawo! Inuyo simuchoka, mpaka wamng’ono wanuyo atabwera kuno.

16-Tumani m’modzi wa inu kuti apite akamutenge. Ena nonse otsalanu mukhale mu ndende ndithu, mpaka mawu anuwa atsimikizike, tiwone ngati mukunena zowona. Apo ayi, ndithu pali Farawo, inuyo ndinu azondi basi.”

17-Atanena mawu amenea, anakaatsekera mu ndende masiku atatu.

-Yosefe anaakumbukira abale ake aja koma iwowo sankamukumbukira iye.



ndipo chimodzi mwa zigawo zisano zilizonse za zokolola, azichiyika padera pa zaka zisano ndi ziiri za chakudya chochuluka.

35-Asonkhanitse chakudya chonse cha zaka za zinthu zimene zikubwerazi. Azichita zonsezi ndi ulamuliro wanu, ndipo aziika tiligu padera m’mizinda yonse ndikumusunga bwino.

36-Chakudya chimenecho chidzakhala chakudya cha nthai ya njala ya zaka zisano ndi ziiri imene idzabwere ndithu mu Ejipito muno, chomcho kuti anthu a ku Ejipito asadzafe ndi njala.”

-Yosefe anaganiza kuti Farawo amufune munthu wina amene adzisunga zakudya kuti anthu adzakhale ndi zakudya mu nthai ya njala.

-Kodi Farawo anaganiza zotani pa maganizo a Yosefe?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:37-40

37-Farawo pamodzi ndi nduna zake anavomereza zimene ananena Yosefe.

38-Tsopano Farawo anazifunsa nduna zakezo kuti, “Kodi tingamupeze kuti munthu wina oposa uyu amene ali ndi mzimu wa Mulungu?”

39-Chomcho Farawo anamuwuza Yosefe kuti, “Popeza kuti Mulungu wakuwonetsa zonsezi, palibenso wina aliyense odziŵa zinthu ndiponso wa nzeru kupambana iweyo.

40-Iwe ndi amene udzalamulire dziko langa, ndipo anthu anga onse adzakumvera. Ine ndidzakupambana pa chokhachi chakuti ine ndi mfumu.”

-Farawo anamusankha Yosefe kukhala nduna yayikulu kwambiri ku Ejipito.
-Farawo yekha ndi amene anali wamkulu kwa Yosefe ku Ejipitoko.

-Ngakhale kuti Yosefe anagulitsidwa ndi abale ake ngati kapolo, Mulungu sanamutaye Yosefe.
-Ngakhale kuti Yosefe anayikidwa mnyumba ya ukaydi, Mulungu samutaye Yosefe.

-Kodi Mulungu anaakwanilitsa bwanji maloto amene anamupatsa Yosefe ali mwana aja?
-Mulungu anamusankha Yosefe kukhala nduna yayikulu kwambiri ya dziko lonse la Ejipito.
-Mulungu amachita zimene waganiza.
-Palibe munthu amene angathe kuziletsa zimene wakhoza Mulungu.

-Pamene Farawo anamusakha Yosefe kukhala nduna yayikulu kwambiri m'dziko la Ejipito, Yosefe anayamba kusunga zakudya zabwino za zokolora zimene zinkatsala.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 41:46-49

46-Yosefe anali ndi zaka makumi atatu pamene anayamba kumugwilira ntchito Farawo, mfumu ya ku Ejipito. Ananyamuka, nayendera dziko lonse.
47-Pa zaka za zokolola zambiri zija, m'dziko lonse munali chakudya chochuluka kwambiri.
48-Yosefe anasonkhanitsa chakudya pa zaka zisano ndi ziiri, pamene kunali zokolola zochuluka kwambiri ku Ejipito, nazisunga m'mizinda. Mu mzinda uliwonse amkasunga chakudya cha ku minda yozungulira mzindawo.
49-Anasonkhanitsa tiriigu wochuluka ngati mchenga wa ku nyanja. Kunali tirigu wochuluka kwambiri kotero kuti analeka nkumuyesa komwe, popeza kuti kunali kosatheka kumuyesa tirigu yenseyo.

-Mu zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri, Yosefe anasunga zakudya zambiri zosaerengeka.



-Zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri zitatha, zaka zisano ndi ziiri za njala zinayamba.

-Kodi bambo ake a Yosefe pamodzi ndi abale ake ankakhala kuti?
-Ku Kanani.

-Ku Kenani, nakonso kunali njala ndipo bambo ake a Yosefe pamodzi ndi abale ake analibe zakudya.

-Apa pali zimene analankhula bambo ake a Yosefe:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 42:1-5

1-Yakobo atamva kuti ku Ejipito ndiko kuli tirigu wambiri, anaŵafunsa anaake kuti, "Chifukwa chiyani mukungokhala osachitapo kanthu?
2-Ndikumva kuti ku Ejipito kuli tirigu. Pitani kumeneko, mukatigulireko ife, kuti tingafe ndi njala."
3-Chomcho abale ake a Yosefe khumi ananyamuka kupita ku Ejipito kukagula tirigu.
4-Yakobo sanamutume nawo Benjamini, mng'ono wake weniweni wa Yosefe uja, chifukwa chakuti amkawopanso kuti angapeze tsoka.
5-Ana a Isilayeliwo anapita ku Ejipito kukagula chakudya pamodzi ndi anthu ena onse, chifukwa chakuti ku dziko la Kanani kunali njala.

-Bambo ake a Yosefe anaatumiza ana awo amuna ku Ejipito kukagula zakudya.

-Kodi chinachitika ndi chiyani abale ake a Yosefe aja atafika ku Ejipito?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 42:6b-17